



Ndondomeko Ya Chuma Cha Boma 2021-22



Photo: © UNICEF/2020/Chikondi

1. CHUMA CHA DZIKO LA MALAWI

Chuma cha dziko lino chomwe chinali ndi chiyemebekezo chokwera ndi 1.9 peresenti chinakwera ndi 0.9 peresenti mu chaka cha 2020-21. Chumachi koma chikuyembekezereka kukwera ndi 3.8 peresenti mu chaka cha 2021 komanso kukwera ndi 5.2 peresenti mu chaka cha 2022. Izi zili chomwechi chifukwa chakukwera kwa ntchito za ulimi komwe kukuyenera kukwera ndi 6.2 peresenti mu chaka cha 2021. Magawo ambiri a zachuma nawo akuyembekezereka kukwera mu chakachi.

Pali chiyembekezo choti mitengo ya zinthu mu dziko muno ifika pa 7.5 peresenti mu 2021 komanso 7.3 peresenti mu chaka cha 2022. Koterokuti malingaliro a Boma wotsitsa mitengo kufika pa 5.0 peresenti mu 2022 komaso kufika pa 3.0 peresenti mu chaka cha 2025 adzakwaniritsidwa.

2. NDONDOMEKO YA CHUMA YA MU CHAKA CHA 2021-22

Ndondomeko ya chaka cha 2021-22 ikhala yamiyezi isanu ndi inayi chifukwa chakusinthwa kwa chaka cha chuma cha boma chimene chidziyamba pa 1 April kuyambira mu chaka cha 2022.

2.1 THUMBA LA CHUMA CHIMENE CHIKUYEMBEKEZEREKA KUPEZEKA MU CHAKACHI

Ndalama zonse zimene Boma likuyembekezera kupeza mu chaka cha za chuma cha 2021-22 ndi K1,271.26 biliyoni zomwe ndi 12 peresenti ya Chuma chonse cha dziko la Malawi (GDP). Mwa ndalamazi, K1,100.95 biliyoni ikuyembekezereka kuchokera mu dziko momwe muno, pamene K170.31 biliyoni ndi chithandizo chimene ikuyembekezereka kuchokera ku mayiko ndi ma bungwe akunja. Mwa ndalama za mdziko momwemuno, 82 peresenti ikuchokera ku misonkho, pamene zotsalazo zikuyembekezereka kuchokera ku madera ena kuphatikizirapo mayiko ndi mabungwe akunja kwa dziko lino.

Mu chaka cha 2021-22, boma likuyembekezera kupeza ndalama zokwanira K1,044.05 biliyoni kuchokera ku misonkho zomwe ndi zocheperako ndi 6.5 peresenti keyerekeza ndi zomwe boma llinapeza mu chaka cha 2020-21.

Munthawi yomweyi, nazo ndalama zimene boma likuyembekezera kupeza mdziko lino kudzera munjira zina kupatulapo misonkho zikuyembekezereka kutsika kufika pa K56.9 biliyoni kuchoka pa K63.1 biliyoni mu 2020-21 komwe ndikutsika kwa 10.9 peresenti. Izi zili chomechi kamba ka kusitha kwa chaka cha boma.


Mwa ndalama zomwe zingachokere kunja zokwana K170.31 biliyoni, ndalama zokwana K58.43 biliyoni zidzachokera ku mayiko monga Norway, Germany, ndi Ireland. Pamene K111.88 biliyoni zidzachokera ku mabungwe akunja monga Banki la Dziko lonse lapansi, Mgwirizano wa mayiko aku Ulaya, ndi Bungwe la kunja lohandiza chitikuko cha ulimi (International Fund for Agriculture Development). Ndalamazi ndi zotsikirapo ndi 50 peresenti, kuyerekeza ndi zimene mabungwe ndi mayikowa anapereka mu chaka cha 2021-22.

2.2 KAGWIRITSIDWE NTCHITO KA NDALAMA


Mu chaka cha 2021-22, Boma likuyembekezereka kugwiritsa ntchito ndalama zokwana K1,995.1 biliyoni zomwe ndi 19.4 peresenti ya chuma chonse cha mu dziko lino (GDP) Ndalamazi ndi zotsika ndi 9.2 peresenti kuyerekeza ndi zimene Boma linavomerezedwa kugwiritsa ntchito mu chaka cha 2021-22 zomwe zinali zokwana K2,190.18 biliyoni. Mwa ndalamazi za mu chaka cha 2021-22, K1,424.3 biliyoni zigwiritsidwira poyendetsa ntchito za Boma za tsiku ndi tsiku monga momwe zikuwonekera mu chithunzi 2.

Ndalama zokwanira K570.84 biliyoni (28.7 peresenti) zigwiritsidwa ntchito za chitikuko ndipo K219.60 biliyoni ya ndamalazi zichokere mu dziko momwe muno, pamene ndalama zokwana K351.24 biliyoni zichokere ku mayiko ndi ma bungwe akunja.

CHITHUNZI 1



CHITHUNZI 2



2.3 NDALAMA ZOBWEREKERA MU 2021-22

Mu chaka cha 2021-22, ndalama zomwe Boma lidzapeze zidzakala zocheperapo ndi K723.8 bilyoni poyerekeza ndi ndalama zomwe zikufunika kugwira ntchito m'chakachi. Choncho Boma lidzafunika kubwera ndalama zokwana K134.8 bilyoni kuchokera kunja komanso K589.1 bilyoni kuchokera mu dziko momwe muno.

Mu chaka cha 2021-22, ndalama zomwe Boma lidzapeze zidzakala zocheperapo ndi K723.8 bilyoni poyerekeza ndi ndalama zomwe zikufunika kugwira ntchito m'chakachi.

TEBULO 1 NDONDOMEKOYA CHUMA (MK' MILIYONI) YA MCHAKA CHA 2021-22

Category	2020-21 Approved	2020-21 Revised	2021-22 Estimates
Ndalama zones zolowa	1,435,051	1,523,376	1,271,261
Zamdziko mommuno	1,179,345	1,185,829	1,100,946
Misokho	1,116,265	1,116,265	1,044,051
Zimphaso ndi zindapusa	63,080	69,564	56,895
Zithandizo	255,705	337,547	170,314
Zochokera kumayiko akunja	34,755	40,178	58,430
Zochokera ku mabungwe akunja	220,950	297,369	111,884
Ndalama Zogwiritsa Ntchito	2,190,180	2,335,053	1,995,101
Zogwiritsira ntchito tsiku ndi tsiku	1,678,993	1,719,213	1,424,263
Zopita kwa ogwira ntchito m'boma	538,018	542,157	449,615
Malipiro	523,680	525,280	436,324
Za opuma pa ntchito	14,338	16,877	13,290
Chiwongola dzanja	376,014	376,014	299,728
Pa ngogole zotengedfwa kunja	11,854	11,854	14,474
Pa ngongole zotengedwa m'dziko mommuno	364,160	364,160	285,254
Zogulira katundu ndi upangiri	309,211	347,065	269,642
Katundu ndi Upangiri	185,169	223,829	164,769
Za umoyo	60,145	59,625	49,026
Za ulimi	7,550	7,350	4,989
Za maphunziro	35,045	34,205	29,783
Ngongole zokhalitsa (Arrears)	7,000	7,000	5,000
Zolipira mosungira mafuta (Storage levy expenses)	2,984	2,984	2,875
Zogulira chimanga kwa alimi	10,000	10,353	12,000
Za chisankho	1,318	1,718	1,200
Ndalama zothandizira ma bungwe	177,240	184,181	154,000
Zopita ku makampani a boma	177,240	184,181	154,000
Bungwe lalipira miseu (Roads Fund)	33,991	33,991	31,332
Bungwe lomanga miseu (Roads Authority)	4,416	4,416	3,312
Bungwe Lotolera Msokho (MRA)	32,396	32,396	30,992
Makampani wothanizidwa ndi boma (Subvented Organisations)	97,437	104,378	79,363
Zobwereketsa (Net Lending)	9,000	9,000	9,000
Zothandizira anthu	266,010	248,250	221,825
Zipangizo za ulimi zotsika mtengo	160,169	141,996	141,988
Za malipiro a anthu opuma pa ntchito	102,840	103,254	77,588
Mtukula pakhomu	3,000	3,000	2,250
Zolipira zina ndi zina	12,500	21,547	29,453
Zachitukuko	511,188	615,840	570,838
Zamayiko ndi mabiungwe akunja	410,295	511,129	351,243
Za mmomuno	100,893	104,711	219,595
Ngongole	755,130	811,677	723,840
Zochokera kunja	224,779	246,265	134,774
Zamdziko mommuno	530,351	565,412	583,544

3. KAGAWIDWE KA NDALAMA KU MA GAWO AKULUAKULU A NTCHITO ZA BOMA

3.1 MALIPIRO A ANTHU WOGWIRA M'BOMA

Ndalama zokwana K436.32 bilyoni mu ndondomeko ya ndalama zoyendetsera boma za 2021-22 zigwiritsidwa polipira anthu ogwira ntchito M'boma kwa miyezi isanu ndi inayi. Izi ndi zotsikrapo ndi 16.7 peresenti kuyerekeza ndi za miyezi khumi ndi iwiri za mu chaka cha 2020-21 zomwe zinali K523.68 bilyoni.

3.2 NTCHITO ZA TSIKU NDITSIKU ZA BOMA

Ndalama zonse zomwe Boma lidzagwiritse kuyendetsera ntchito tsiku ndi tsiku ndi zokwana K987.9 bilyoni zomwe ndi zotsika ndi 14.9 peresenti kuyerekeza ndi zimene zinavomerezeka kugwira ntchito ngati yomweyi mu chaka cha 2020-21. Chithunzi 3 chikuwonetsa ma gawo ake omwe ndalamazi zidzagwire ntchito.

3.3 ZACHITUKUKO

Ntchito zachitukuko zapatsidwa ndalama zokwana K570.8 bilyoni imene ili yokwera ndi 11.7 peresenti poyerekeza ndi za m'chaka cha 2020/21 zimene zinali K511.2 bilyoni. Mwandalama za 2021-22, K351,2 bilyoni zachiokera ku mayiko ndi mabungwe a kunja pamene K219.6 bilyoni zikochokera mdziko mmomuno.

4. KAGAWIDWE KA NDALAMA MOLINGANA NDI NSANAMIRA NDI ZOYENEREZA ZA MASOMPHENYA A ADZIKO LINO A 2063


4.1 KAGAWIDWE KA NDALAMA KU NSANAMILA

Kagawidwe ka ndalama mu ndondomeko ya chuma cha 2021-22 ku nsanamila za masophenya a dziko lino a 2063 ali motere: 12 peresenti ya yaperekedwa ku za ulimi, 3 peresenti zomangira mizinda yapamwamba ndipo 2 peresenti ku zotukula mafakitale ndi migodi.

4.2 KAGAWIDWE KA NDALAMA KU ZOYENEREZA


Kagawidwe ka ndalama mu ndondomeko ya chuma cha 2021-22 ku Zoyenerenza za masomphenya a dziko lino a 2063 ali motere: 32 peresenti yapita ku chitukuko cha anthu paluso logwirira ntchito, 29 peresenti ku kulimbikitsa kagwiridwe ntchito ka m'boma, 9 peresenti ku kayendetsedwe kabwino ka boma, ndi 9 peresenti ina ku chitukuko za chuma.

CHITHUNZI 3



Kagawidwe ka ndalama mu ndondomeko ya chuma cha 2021-22 ku nsanamila za masophenya a dziko lino a 2063 ali motere: 12 peresenti ya yaperekedwa ku za ulimi, 3 peresenti zomangira mizinda yapamwamba ndipo 2 peresenti ku zotukula mafakitale ndi migodi.


CHITHUNZI 4



5. MAGAWO AKULU AKULU MU NDONDOMEKO YA CHUMA CHA BOMA OKHUDZA NZIKA


Ena mwa magawo akulu akulu omwe apindulire nzika mu Ndongomeko ya chuma cha 2021-22 ali motere.

CHITHUNZI 5



MAGAWO A NDONDOMEKZA YA CHUMA CHA BOMA WOKOMERA A MALAWI ONSE (MK, BILIYONI)

MAPHUNZIRO NDI UMISIRI



3.5 yapita ku nkondo yolimbana ndi matenda a Covid-19 mu gawo la maphunziro

3.6

ipita kuntchito yowonetsetsa kuti ophunzira amene amaliza sukulu aphunzire ntchito m'boma ndi mabungwe aboma

9.0

ithandizira wophunzira womwe sangathe kulipira sukulu ku sukulu za ukachenjede kuti apeze ngongole

21.7

idzagwira ntchito zoyendetsera sukulu za pulayimale ndi sekondale kumanso kugula zipangizo za sukulu

52.5

yapita ku sukulu za ukachenjede

UMOYO WA THANZI



5.0

yapita kunkhondo yolimbana ndi matenga a Covid-19 mu gawo la za umoyo

2.0

ndi yogulira magalimoto otengera anthu wodwala ndi apangozi (Ambulansi)

20.0

ku zipatala za mdziko muno.


6.0

ndi yomangira zipatala

(MK8 biliyoni ku zipatala zazikulu ndi MK12 biliyoni ku makhonzolo)



CHITUKUKO CHA ULIMI, ULIMI WAMTHILIRA NDI CHA MADZI



141.9

yapita ku fetereza otsika mtengo yemwe adzaperekedwe ku ma banja **3.5 miliyoni** a mdziko muno pa mtengo wa **K4,595** yokha pa thumba limodzi

31.6

yaperekedwa ku ntchito za madzi ndi ukhondo

28.9

biliyoni yapita ku chitukuko ya ulimi othilira

12.0

idzagwiritidwa ntchito yogulira chimanga kwa alimi

CHITUKUKO CHA KUMIDZI



56.5

dzagwira ntchito zotukula kumidzi

7.7

yapita ku thumba la chitukuko cha mmadera a Phungu a nyumba ya Malamulo (CDF)

2.8

yapita ku thumba la chitukuko cha mmakhonsolo (DDF)



23.3

idzagwira ntchito zomangira miseu mmizinda

ZOSAMALIRA ANTHU



5.7

apita ku Unduna owona kuti pasakhale kusiyana pakati pa a amayi ndi abambo; komanso ku nthambi za undunawu zomwe zili mma Boma ang'onoang'ono

0.8

yapita kuntchito zothandizira ndi kuteteza anthu akhungu la chilubino komanso anthu a ulumali

2.3

gwira ntchito za madzi kuphatikizapo kubowola mijigo



MTENGATENGA NDI MTKOKOMA



94.5

igwira ntchito yomanga miseu

31.3

igwira ntchito yokonza miseu yowonongeka

Kufuna kumva zambiri: Mlembi wa Ku Unduna wa za Chuma, PO Box 30049, Lilongwe. Lamy pa: +265 (0)1 789 355 Fax pa: +265 (0)1 789 173 E-mail pa: budget@finance.gov.mw

www.finance.gov.mw



Government of Malawi

unicef
for every child